

Tito : 2:1-15

**Mutu : Mpingo uyenera kukhala ndi chiphunzitso
choyenera**

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero tiyamba ndi mau apa a Hebri 10:21-22, amene akuti, “Ndipo popeza tiri naye wansembe wamkuru wosunga nyumba ya Mulungu; tiyandikire ndi mtima woona, m’chikhulupiriro chokwanira ndi mitima yathu yowazidwa kutichotsera chikumbumtima choipa ndi matupi athu osambitsidwa ndi madzi oyera.”

Tsono mupologalamu yatha tinali kusanthula Tito 1:8-2:1, m’mene timakambirana za kuphunzitsa akuru/atsogoleri mu mpingo wokhazikika. Koma lero mu Tito 2:1-15, tikambirana nkhani yakuti mpingo uyenera kukhala ndi chiphunzitso choyenera.

Tito 2

Paulo mu chapter chino, akunena kuti mpingo uli ndi udindo wopereka chiphunzitso choona, kotero kuti ngati mpingowosungathe kuphunzitsa chimenechi, ndiye kuti si mpingo

umenewu. Pamene tiwerenga Machitidwe Atumwi 2:42, tipeza kuti anthu amene anaonjezeka pa tsiku la Pentekoste, anapitiliza kukhala m'chiphunzitso cha Atumwi, kukhala m'chiyanjano, pakunyema mkate ndi m'mapemphero. Izi, ndizo zimene zinali zizindikiro za mpingo woyamba uja. Koma Uthenga ukunena kuti palibe kanthu kukhala ndi mpingo wotchuka kapena wokongola kwambiri, koma chinthu chofunika kwambiri ndi Uthenga womwe umachokera pagome la mpingowo. Ichi, ndichimene Paulo anaphunzira monga momwe mau a Mulungu anena.

Tsono mu chapter 1, tidaona kuti akulu amene Tito amayenera kuwakhazikitsa, amayenera kuchita zinthu ziwiri: kuphunzitsa choona ndi kutsutsa chiphunzitso chonama. Ndiye Paulo akunena kuti sibwino utumiki kungokhazikikapakutsutsa ziphunzitso zonama kokha, chifukwa ulipoutumiki wina, umene umangotsutsa zinthu ziri zonse za utumiki wa Uthenga Wabwino. Koma payenera kukhala utumiki wambali zonse. Kutanthauza kuti m'busa pampingo, ayenera kukhala ndi nthawi yokwanira kuphunzitsa Uthenga Wabwino, komanso kutsutsa ziphunzitso zonyengapogwiritsa ntchito mau a Mulungu. Tere, ndichifukwa

chake m'chapter chino, Paulo akulimbikitsa kuti mau a Mulungu ndiwo amene ayenera kuphunzitsidwa mokwanira.

1. Koma lankhula zimene ziyenera chiphunzitso cholamitsa.

Mu chapter 1, Paulo akulangiza Tito momwe angasankhire anthu amene akhoza kutsogolera mpingo. Koma m'chapter chino akupereka malangizo apadera a momwe iye angaperekere Uthenga woona ngati m'busa.

Paulo akunena kuti pamene Tito adzoza kapena kukhazikitsa ena m'maudindowotsogolera mpingo, sizikutanthauza kuti iye, asiye kulalikira Uthenga Wabwino ayi. Koma ayeneranso kupereka upangirikwa akristu onse kuti sayenera kumvera za aphunzitsi onama. Iwo, akhale pachiphunzitso cha Uthenga Wabwino, chimene ndi chobvomerezeka ndi mau a Mulungu, amene alibe chodetsa china chilichonse.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna kunenetsa kuti, atumiki a Mulungu, ayenera kusamalitsa kuphunzitsa zinthu zokhazo zomwe ziri zoona. Kodi abusa anu, mumawakhulupirira kuti

amaphunzitsa mau a Mulungu?Kapena kuti mpingo wanu uli ndi chiphunzitso choyenera chomwe chichokera m'mau a Mulungu?

2. Okalamba akhale odzisunga, olemkezeka, odziletsa, olamam'chikhulupiriro, m'chikondi, m'chipiriro.

Paulo akumuza Tito, kuti chiphunzitso choyenera, chiyenera kukhudza gulu lililonse la anthu, malinga ndi misinkhu yawo.Kutanthauza kuti m'busa ayenera kuona chakudya chomwe ndi choyenera cha gulu lililonse.Ndiye akunenanso kuti pamene apatula kuphunzitsa gulu lililonse palokha, ayeneranso kukhala chitsanzo monsemo.Tito amayenera kuphunzitsa gulu la anthu onse ntchito yawo.Monga gulu la okalamba ndi anyamata, komanso gulu la amuna ndi akazi, la ophunzitsa ngakhaleenso la akapolo.

Ndiye mundime ino, Paulo akumuza kuti anthu akulumisinkhu, ayenera kukhala ndi makhalidwe okoma. Kunena kuti pamene thupi lawo likufookaiwo sayenera kutailira m'makhalidwe awo. Mwanjira ina, akuru asaganize kuti kukalamba ndi chilolezochakuchita zoipa ayi.Iwowa, ayenera kukhala ndi malankhulidweokoma ndi zizolowezi zabwino.Koma choposa kwambiri ndi chakuti akuruwa ayenera kuimabe pa chikhulupiriro

choona cha Uthenga Wabwino. Asakhale otengeka ndi ziphunzitso kapena miyambo ina ayi. Kutsimikiza kuti anthu amene aliakulumisinkhu, ayenera kukhala wodzazidwa ndi chisomo ndi kukomamtima, kotero kuti munthu wamkati, ayenera kumakhala watsopano ngakhale pamene thupi lawolikukalamba. Kutsindika kuti munthu wokalamba ndiye amene ayenera kuphunzitsidwa kukonda Ambuye pamodzi ndi anthu ena omwe. Ichi, ndichimene chingapangitse anthu ena kuwalemekeza ndi kuwakhulupirira.

3. Momwemonso akazi okalamba akhale nawo makhalidwe oyenera anthu oyera, osadierekeza, osakodwa nacho chikondi cha pavinyo, akuphunzitsa zokoma.

Nawonso akazi okalamba, ayenera kukhala woyera m'makhalidwe awo, kuti akwaniritse chikhulupiriro chawo pa Ambuye. Akazi nawonsomonga amuna, ayenera kuphunzira ndi kuchita zinthu zomwe amuna ayenera kuchita, popeza njira yachipulumutso ndi imodzi. Komanso ayenera kukhala aphunzitsia ntchito zabwino. Kutsimikiza mau apa 1 Akorinto 10:31, amene akuti, “Chifukwa chake mungakhalemudya, mungakhalemumwa, mungakhalemuchita kanthu kena, chitani zonse ku ulemerero wa

Mulungu.” Kodi inu mumakwanitsa kuchita chilichonse kuulemererowa Mulungu?

4. Kuti akalangize akazi ang’onoakonde amuna awo, akonde ana awo.

5. Akhale odziletsa, odekha, ochita m’nyumba mwawo, okoma, akumvera amuna a iwo wokha, kuti mau a Mulungu angachitidwe mwano.

Pano ndifuna kuyamba ndi mau akuti, kukhala mkazi wapanyumba ndi udindo waukulu popeza amayang’anira nyumba yonse pamodzi ndi ana omwe. Tikunenetsa kuti sichinthuchapafupikusenza udindo umenewu, popeza ayenera kukhala tcheru pa zinthu zonse zokhudza banja lake. Tsono chipembedzo ndicho chimene chiyenera kumayang’anira ndi kupereka nkhani zonse ndi makhalidwe oyenera apa banja. Kutanthauza kuti chipembedzo ndicho chimene chimapanga banja, kukhala nyumba yamtendere, yokwanira ndi yoyenera kukhalapo. Pachifukwa chimenechi, banja silikhala lokoma ngati udindo wa anthu apa banjalowaiwalika ndi kutaika. Kutsimikiza kuti pa ntchito zonse zimene amuna kapena akazi agwira, ayenera kudziwa

kuti udindo wawo woyamba uli panyumba kotero kuti ngati udindo wapa nyumba ugwirika bwino, ntchito zina zonse zidzayendanso bwino. Ndichifukwa chake Paulo pa Aefeso 5:21, akunenetsa kuti, “Ndikumverana wina ndi mnzake m’kuopa Kristu.” Kutanthauza kuti mwamuna ndi mkazi ayenera kumveranapogwira ntchito zonse za pa banjapo.

6. Momwemonso anyamatauwadandaulire akhale odziletsa.

7. M’zonseudzionetsere wekha chitsanzo cha ntchito zabwino; m’chiphunzitso chako uonetsererechosabvunda, ulemekezeko,

Tsopano Paulo watembenukirakwaanyamata, kunena kuti Tito, ndiye amene ayenera kuwaphunzitsa iwowa. Paulo akunena kuti anyamata ayenera kukhala wosamala ndi kuchenjerapakulamulira zokhumba za mtima wawo. Tsono kuti mnyamata akhale ndi ulamuliro wabwino pamoyo wake, ayenera kukhala ndi chidziwitso cha mau a Mulungu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, Paulo akuona kuti anyamata ayenera kuphunzitsidwa bwino m’chiphunzitso choona pazifukwa izi; Poyamba tikuona chifukwa chakuti chiyembekezo cha mpingo chagona pa iwowa. Kachiwiri, mnyamata amene sangathe

kudziyang'anira bwino, amapereka chiyembekezo chochepa kuti akhoza kukhala munthu wofunika ndi wokonda Mulungu. Kachitatu, tikuona kuti ndikoyenera kuphunzitsa mnyamata mau a Mulungu chifukwa akhoza kuononga moyo wake mosabvuta pamene alowam'zizolowe zizachabe. Komanso pomalizamnyamata monga munthu wina aliyense, ayenera kukhala ndi chiyembekezo chakuti adzafa ndipo kuti afunitsa kukakhala m'moyo wachisangalalo kwamuyaya. Ndiye Paulo akulimbikitsa Tito, kukhala m'moyo wachitsanzo chabwino, kuti akhoze kuphunzitsa anyamata anzake. Kunena kuti pamene Tito aphunzitsa, ayenera kuonetsa moyo wokonda Mulungu ndi wokhulupirika. Kutanthauza kuti ayenera kuonetsa kufunika kwa zinthu zomwe iye akuphunzitsa.

8. Mau olamaosatsutsika; kuti iye wakutsutsana achite manyazi, posakhala nako kanthu koipakakutineneraife.

Tito pano akulangizidwa kuti iye, ngati m'busa ayenera kupereka mau amene ndi wopatsa moyo wauzimu. Mwanjira inaakulangizidwa kuphunzitsa mau a Mulungu oona, amene akhoza kukweza dzina la Mulungu, kupititsa patsogolo cholinga

cha Ambuye Yesu Kristu ndi Ufumu wake ndikutengera chisangalalo miyoyo yochuluka. Kutsimikiza kuti mau a Mulungu ayenera kulalikidwa osati pachifukwa chofuna kudziphezera ulemu ndi cholowa ayi, koma kukwaniritsa cholinga cha moyo wauzimu. Awa, ndimau amene akulankhula Paulo pa 1 Timoteo 4:16, pamene akuti, “Udzipenyerere wekha ndi chiphunzitsocho. Uzikhala mu izi; pakuti pochita ichi, udzadzipulumutsa iwe wekha ndi iwo akumva iwe.” Kutsimikiza kuti m’busa kapena mtsogoleri alalikire choona chomwe chidzathandiza ena pamodzi ndi moyo wake womwe. Koma akunena kuti moyo kapena zochita za m’busa kaya mtsogoleri ziyenera kugwirizana ndi mau amene amaturuka pakamwa pake.Kodi inu ngati m’busa kapena mkuruwampingo mau oturuka pakamwa panuamagwirizana ndi zomwe inu mumachita?

9. Akapolo amvereambuye awo a iwookha, nawakondweretsem’zonse; osakana mau awo.

Tsopano Paulo watembenukirakwa akapolo kapena gulu la anthu ogwira ntchito. Mumpingo woyamba munali akapolo ambiri, amene anali kutumikira ambuye awo.Ndiye Uthenga Wabwino ndiwo unali

wofunika kwambiri kugulu la anthu amenewa.Tsono Paulo akunena kuti Tito, aphunzitse kuti anthu amenewa ayenera kukhalawomveraambuye awo ndi kuchita zinthu mowakondweretsa.Pfundo ikuti akapolowa kapena kuti anthu olembedwa ntchito, ayenera kuchita monga ambuye kapena owalemba ntchito afuna.Izi, zikhoza kuchitika pamene akapolowaasonyeza mtima wokonda ndi kukhala ndi chidwi pa ntchito yawo.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani ili pano ikunena kuti anthu onse olembedwa ntchito, maka-maka ife akristu, tiyenera kuika mitima yathu pantchito yomwe tigwira ndipo ngati sitingakwanitse, ndibwino kusiya ntchitoyo. Kutanthauza kuti ngati inu mulowa ntchito, muyenera kutsimikiza kuti mufunakuigwirantchitoyo.Tikunena kuti ngakhale ntchitoyoiyenerakukuthandizani pamoyo wanu watsiku ndi tsiku, akristu ayenera kugwira ntchito ndi mtima, mutu ndi manja awo omwe.Kutanthauza kugwira ntchito modzipereka. Mwanjira ina tikunenetsa kuti wokhulupirira sayenera kusanjula mau ya mbuye wake ayi. Kutsimikiza mau a Paulo pa Akolose 3:23, amene akuti,

“Chiri chonse muchichita, gwirani ntchito mochokera mumtima, monga kwa Ambuye, osati kwa anthu ayi.”

10. Osatapa pa zawo, komatu aonetserekhulupiriko chonse chabwino; kuti akakometsere chiphunzitso cha Mpulumutsi wathu Mulungu m’zinthu zonse.

Pamene Paulo akunena kuti “Osatapa pa zawo,” akunena kuti kapolo asabe. Iwowa, aonetse kukhulupirika ngakhale kuti anthu ambiri akuchita chimenechi. Kutsimikiza kuti wogwira ntchito ali ndi udindo wokweza ndi kukometsa chiphunzitso cha Mulungu, amene ndi Mpulumutsi. Tere inu ndi ine, tiyenera kulankhula ndi kugwira ntchito ndi cholinga chokometsa dzina la Ambuye. Kutsindika kuti wogwira ntchito sayenera kugwira ntchito kwa mbuye wake wapansi pano, koma ayenera kuika maso ake kwa Mbuye wa m’Mwamba. Ndiye Paulo akulangiza kuti, atumiki a mau a Mulungu nawonso, ayenera kupereka Uthenga monga momwe Mulungu afuna, osati kukwaniritsa zofuna ndi zosowa zawo ayi.

11. Pakuti chaonekera chisomo cha Mulungu chakupulumutsa anthu onse,

Tsono Paulo mundime ino, akufuna kukhazikitsa maziko ya moyo wa a Krete, mwanjira yowabweretsapachiphunzitso cha chisomo cha Mulungu popeza ndicho chofunika kwambiri. Pamene tikamba za chisomo cha Mulungu, ndiye kuti tiri pankhani yanjira yomwe Mulungu anakhazikitsa kuti munthu wochimwa apulumutsidwe. Tamvani a Dr. Dodd, adanena kuti, “Uthenga Wabwino si mau aupangiri, koma ndi mau abwino, amene ali ndi mphamvu ya Mulungu yopulumutsa.”

Ichi, ndichimene Paulo akufulumiza Tito, kuti aphunzitse a Krete, kukhala m'moyo wokweza Uthenga Wabwino, popeza ndiwo mphamvu ya Mulungu. Kutanthauza kuti palibe chifukwa chakuti munthu wokhulupirira akhale m'moyo wofooka ndi wogonja pamene chisomo cha Mulungu chinadza ndi chipulumutso kwa anthu onse.

Tsono pamene Paulo akunena kuti, “Chisomo chaonekera,” akukamba nkhani yakubwerakwa Ambuye Yesu, m'zaka zoposa 2,000, umene uli Uthenga Wabwino. Taonani Ambuye Yesu anafa chifukwa cha ife ndipo anauka kwa akufa. Kunena kuti Mulungu sapulumutsa munthu chifukwa cha chikondi kapena chifundo ayi,

koma chifukwa cha chisomo monga Paulo akunena pa Aefeso 2:8, pamene akunena kuti, “Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi chosachokerakwa inu: chiri mphatso ya Mulungu.”

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna mundimvetsetse kuti, chifundo ndichomwechinakakamiza Mulungu kutumiza Mpulumutsi kwa munthu wotaika. Kutanthauza kuti ngati munthu m’modzi akanapulumuka ndi chifundo ndiye kuti anthu onse apa dziko lapansi, akapulumutsidwa. Kunena kuti sikunali koyenera kuti Kristu afe m’malo mwa anthu onse ayi. Tikunena kuti mtandasukanagwira ntchito. Ndiye tikunenetsa kuti Mulungu anakonda anthu, koma sadagwiritse ntchito chikondi pakupulumutsa munthu ayi, anagwiritsa ntchito chisomo. Ichi, ndichinthu chochititsa chidwi kuti ife tikhoza kupulumutsidwa mwachisomo cha Mulungu. Tikunena kuti pamene ife, tinali chikhalire muuchimo wathu, Kristu analipadipo la uchimo wathuwo. Kutsimikiza kuti Mulungu safuna kuti inu mugwiritse ntchito nzeru ngakhale mphamvu zanu ayi, koma amangofuna inu kuti mukhulupirire, kumudalira ndi kumulandira Kristu. Tere iyi,

ndinjira yokhayo yopambana yomwe Mulungu anakhazikitsayopulumutsira inu ndi ine. Kodi inu mukhoza kupeza njira ina? Kapena tifunse kuti, kodi palibe njira ina yoposa yomwe Mulungu anakhazikitsa?

12. Ndi kutiphunzitsaife kuti, pokanachisapembedzo ndi zilakolako za dziko lapansi, tikhale ndi moyo m'dziko lino odziletsa, ndi olungama, ndi opembedza.

Pano ndifuna kuyamba ndi mau akuti Mulungu safuna kusintha dziko lino, koma kupulumutsa anthu amene angalandire Kristu. Ndiye tikunena kuti Uthenga Wabwino, ulibe ntchito kapena kuti sungafulumizemunthu wokana Kristu kuchita ntchito zabwino ayi. Tere, ndichifukwa chake Paulo akunena kuti Mulungu afuna ana ake, amene anapulumutsidwa kuti akhale m'moyo wokonda Mulungu osati kukonda zadziko ayi.

13. Akulindira chiyembekezo chodala, ndi maonekedwe a ulemerero wa Mulungu wamkuru ndi Mpulumutsi wathu Yesu Kristu;

Pamene Paulo akunena za “Kulindira chiyembekezo chodala,” akukamba za chinthu chomwe chidzachitika posachedwa mu chikonzero (programme) ya Mulungu. Uku, ndikudzakwa Kristu pamene akudzatenga mpingo wake kuchoka m’dziko lino. Tere, inu ndi ine, tiyenera kuyang’anira ndi kudikira chiyembekezo chodala chimenechi. Kutsindika kuti chithonhozondi chimwemwe cha wokhulupirira ndicho kudziwa kuti Mpulumutsi wawo ndiye Mulungu Wamkuru, amene adzadzionetsa yekha pakudza kwake kachiwiri. Kodi inu chithonhozo ndi chimwemwe chanu chiri mwandani?

14. Amene anadzipereka yekha m’malo mwa ife, kuti akatiombole ife ku zoipa zonse, nakadziyeretsere yekha anthu akhale ake eni eni, achangu pa ntchito zokoma.

15. Izi, lankhula ndipo uchenjeze, nudzudzule ndi ulamuliro wonse. Munthu asakupeputse.

Nkhani ili pano ikuti Kristu anadzipereka yekha kuti atipulumutse ife. Iye, anachita izi, mwakudzipereka yekha dipo m’malo mwathu ndi cholinga chofuna kutipulumutsa kumachimo athu onse. Ndiye pamene tidakhulupirira Iye, tidakhala ake. Tsono tikunena kuti

inu simungakhale ake-ake ndi kumutumikira Iye, pokha-pokha inu mupulumutsidwekaye. Ndiye funso likuti, kodi inu, ndinu ake-ake?

Tiyeni titsirize ndi mau amene Paulo akulimbikitsa Tito, kuti ngakhale iye ndiwamng'ono, a Krete, sayenera kumuderera chifukwa cha moyo wa Kristu umene alinawo. Pachifukwa chiemenechi, Tito ayenera kuphunzitsa ndi ulamuliro wa Kristu. Kodi inu mumapereka Uthenga Wabwino ndi ulamuliro wa ndani?

Lero tilekeza pano. Koma timakambirana pa Tito 2:1-15, pankhani yakuti mpingo uyenera kukhala ndi chiphunzitso choyenera.

Ambuye akudalitseni inu. Amen!